Mtsikana amalandira katemerayu katatu.

- Akalandira oyamba,
- wachiwiri amalandira pakatha miyezi iwiri.
- Omaliza amalandira pakatha miyezi inayi atalandira wachiwiri

Uthenga wapadera:

- Aphunzitsi, onetsetsani kuti atsikana onse a standade 4 alandira katemera wa HPV kuti atetezedwe ku khansa ya khomo lachiberekero
- Aphunzitsi fotokozerani ana zakufunika kolandira katemera wa HPV kuti amvetsetse za katemerayu
- Mafumu limbikitsani anthu anu kukalandiritsa atsikana katemera wa HPV kuti atetezedwe ku khansa ya chiberekero
- Msungwana, dziteteze ku khansa yakhomo la chiberekero. Landira katemera wa HPV.
- Amayi a msinkhu wobereka kayezetseni khansa yakhomo la chibelekero kuti ngati muli nayo muthandizidwe zisanafike povuta
- Makolo fotokozerani ana zakufunika kolandira katemera wa HPV kuti amvetsetse za katemerayu.

Mukafuna kudziwa zambiri, kafunseni kwa adokotala kuchipatala chapafupi ndi inu

Produced by Health Education Unit in collaboration with EPI, RHU, NCD with support from WHO, CHAI, GAVI (2013)

katemera wa khansa ya khomo la chibelekero

Mau oyamba

Unduna wa za Umoyo wakhala ukuona anthu ochuluka odwala matenda a Khansa omwe akumafika kuzipatala zosiyanasiyana. Khansa ndi matenda omwe akhoza kugwira chiwalo chilichonse ndipo wodwala akapanda kupeza chithandizo choyenera msanga, matendawa amafalikira ziwalo zina.

Mwamitundu ya Khansa yonse, khansa yakhomo la chiberekero ndi yomwe ili yochuluka kwambiri mwa amayi. Chaka chilichonse amayi opitirira 2,300 amadwala matendawa ndipo opitirira 1,600 amamwalira.

Chifukwa cha kukula kwa vutoli, boma lakonza ndondomeko yopereka katemera wa Human Papilloma Virus (HPV) kwa atsikana ndi cholinga chowateteza kumatenda a khansa ya khomo la chiberekero. HPV ndi kachirombo komwe kamayambitsa matendawa. Katemerayu ayamba kuperekedwa mu maboma a Rumphi ndi Zomba mu September, 2013.

Kodi khansa ya khomo la chiberekero ndi chiyani?

Iyi ndi khansa yomwe imagwira khomo la chibelerekero. Ngati amayi salandira chithandizo msanga, khomo la chiberekero limawonongeka ndipo kuwonongekako kungathe kumafalikira ziwalo zina.

Ziizindikiro za khansa ya khomo lachibelekero ndi ziti?

- Munthu amene ali ndi khansa ya khomo lachibelekero saonetsa zizindikiro msanga mpakana matenda atakula.
- Mayi amataya magazi akangotha kugonana.
- Kutaya magazi kwa mzimayi amene anasiya kusamba.
- Mayi kutaya magazi nthawi imene sakuyenera kusamba
- Kutulutsa chikazi chochuluka chosintha mtundu, komanso chafungo.
- Kumva kupweteka mchiuno, mwendo ndi msana.

Kodi chimayambitsa khansayi ndi chiyani?

Khansayi imayamba ndi kachirombo kotchedwa Human Papilloma Virus (HPV).

Nanga HPV imafala bwanji?

HPV imafala kuzera mu kugonana

Kodi angatenge HPV ndani?

Aliyense yemwe anayamba mchitidwe ogonana angathe kutenga HPV. Ngakhale kuti wina aliyense angatenge HPV, ndi akazi okha omwe angadwale khansa ya khomo lachiberekero. Munthu yemwe ali ndi HPV samva kupweteka pena paliponse

Kodi zomwe zingapangitse kuti munthuatenge HPV ndi ziti?

- kugonana ndi amuna kapena akazi ambiri
- Kuyamba mchitidwe ogonana ukadali mwana
- Kugonana ndi mwamuna kapena mkazi yemwe amagonana ndi anthu ambiri.
- Kukhala ndi matenda ena opatsirana pogonana.
- Kutsika kwa chitetezo mthupi pa zifukwa zina monga HIV ndi Edzi

Kodi tingapewe bwanji Khansa ya khomo la chiberekero?

- Kulandiritsa atsikana katemera wa HPV
- Kuyamba kuyezetsa khansa ya khomo la chiberekero amayi akakwanitsa zaka 15
- Kupewa kugonana ndi anthu ambiri
- Kugwiritsa ntchito makondomu
- Kupewa mchitidwe ogonana ukadali mwana
- Kuchita mdulidwe wa abambo

Kodi katemera wa HPV amagwira ntchito bwanji?

Katemerayu amateteza atsikana ku kachirombo ka HPV komwe kamayambitsa khansa ya khomo la chiberekero mtsogolo.

Kodi oyenera kulandira katemera wa HPV ndani?

- Katemerayu adziperekedwa mumasukulu kwa atsikana onse a sitandade 4.
- Atsikana omwe sali pa sukulu, ngati akwanitsa zaka 10 adzikalandira katemerayu ku zipatala zonse za boma ndi za mishoni komanso malo onse omwe kumachitikira sikelo ya ana.

Kodi katemerayu amaperekedwa bwanji?

- Katemerayu ndiwobaya pa mkono.